


## ISRAELI NDI MPINGO <sup>5</sup>

 Ndipo usikuuno ife tikufuna kuti tiwayike iwo mu dziko lakwawo. Mulole Ambuye adalitse. Tsopano, mmawa uno ife tinali ndi mafunso ndi mayankho. Mai, ife tinali nawo mulu wa iwo. Ine ndinayamba, ndinayang'ana pafupifupi naini koloko, ndipo timatuluka hafu pasiti thuu, ine ndidakali nalobe thumbalodzadza. Mitundu yonse. Koma mwinamwake ife tikhoza kudzafika kwa iwo sabata yamawa. Akadalipobe ochuluka ali pamwamba pano, ine sindinawawonebe nkomwe, ife tifika kwa iwo mwamsanga momwe ife tingathere. Ndikuyembekeza M'bale Tom adzakhala nafe sabata yamawa. Ndipo kotero ife tiri nawo alaliki ochuluka kuzungulira kuno, ngati mmodzi wa ife akasasa mawu ife tidzangolumphira kwa winayo. Kotero ife. . .

<sup>2</sup> Ino ndi nthawi yanga yoyamba kukhala ndi chitsitsimutso cha mtundu uwu kwa zaka seveni. Zaka seveni zapitazo, sabata ikubwerayi, ine ndinachititsa chitsitsimutso changa chotsiriza kuno ku kachisi. Yakhala ili misonkhano yamachiritso. Ine ndivomereza ife takhala nawo unyinjira wokulirapo ndi zinthu, mpaka kufika handiredi sauzande, koma ine sindinakhalepo ndi nthawi yopambana iliyonse. Ine ndimangokhala ndi nthawi yabwino.

<sup>3</sup> Usiku watha ine ndinali ndikungochucha dovu ngati kavalo akudya msipu, M'bale Wright, kukhala ndi nthawi yodabwitsa! Ambuye anatalitsadi ife.

<sup>4</sup> Iye anatalitsa ife lero mpaka ife tinakhala ngati tikuigwetsera nyumbayo pansu. Izi zikumveka ngati msonkhano wachikale wa msasa, “kuphwasula nyumba,” sichoncho izo? Koma ife tinali ndi nthawi yabwino. Ambuye anatalitsa ife. Ife tikukhulupirira Iye atero usikuuno. Mafunso ena ofunikira kwambiri amene ife tinakambirana m'mawa uno, ena a iwo okhudza nkhani zozama za mu Baibulo.

<sup>5</sup> Tsopano, Lachisanu likubwerali lidzakhala—Uthenga wa kupachikidwa, usiku wa Lachisanu likubwerali, Ambuye akalola, ife tidzamutengera Iye ku mtanda, kukamuwona Iye akupachikidwa, kukamuyika Iye mmanda ndi kukamusunga Iye mmenemo mpaka Loweruka usiku; koma Lamlungu mmawa, pa msonkhano wa Isitara kutuluka kwa dzuwa, ife tidzayesa kuti tidzamutulutsemo Iye, kudzakusonyezani inu momwe Iye amatsimikizira chimene Iye ali.

<sup>6</sup> Zidzakhala zabwino kwambiri, zikadzangotha zimenezo, ngati Ambuye adzatilole ife kudzakhala ndi msonkhano wawukulu wa machiritso, sichoncho izo? Zingadzakhale zokoma. Mwinamwake tidzapeze kodzitamulira kwa high school

kapena chinachake, ndi kudzangowunjikamo masauzande angapo a anthu, ndi kudzakhala ndi msonkhano wawukulu wa machiritso, kudzaziyika izo mu pepala ndi pa wailesi, ndi zina zotero. Kawirikawiri timayendetsamo masauzande angapo a anthu pamene ife tikukhala ndi misonkhano ya machiritso. Ndiko kuitana kwanga, kupempherera odwala. Ndinali ndi chondichitikira chodabwitsa chotero mu mizere imeneyo!

<sup>7</sup> Ndipo ine ndikukhulupirira Ambuye akukonzekera tsopano, chifukwa chimene Iye wandichotsera ine ku munda ndi kudzandikhazika ine pansi, Ine ndikukhulupirira kuti ndi chikumbutso Chake, zaka seveni, Iye adzutsa kadanga kena, kuti ndizipita patsogolo pang’ono. “Pamene mdani abwera ngati madzi osefukira,” Iye anati, “Ine ndidzakweza muyeze wotsutsa izo.”

Usikuuno, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kwa mutu wathu, kapena, kwa Lemba.

<sup>8</sup> Ndipo tsopano tikhala ndi utumiki wa ubatizo ndikangomaliza. Ine sindiyankhula motalika kwambiri usikuuno. Ine ndakhala ndikunena zimenezo usiku uliwonse, kenako nkudzakupatsani inu pafupifupi maora awiri ndi theka, akukhala pamenepo, chilango. Koma ine—ine sindingakhoze kuchita zimenezo usikuuno, chifukwa ine ndiri nawo angapo oti ndiwabatize.

<sup>9</sup> Ndipo mmawa wa Isitala, pambuyo pa msonkhano wa kutuluka kwa dzuwa, udzakhala ubatizo wa mmadzi kuno mu kachisi, aponso, ubatizo wa mmawa wa Isitara.

<sup>10</sup> Iwo adzakhala akubatiza usikuuno. Ndife “abaptisti,” mwa njira ya kubatiza. Ife timangoyenera kukhala Mwamalemba, ndizo zonse. Osati ndendende Achibaptisti; koma Lemba, ife timakhulupirira mu ubatizo mwa kumizidwa. Ndipo, tsopano, ngati inu simukukhulupirira izo mwanjira imeneyo, izo ziri bwinobe. Koma ife timazikhulupirira izo, mu ubatizo wa mmadzi, mwa kumiza.

<sup>11</sup> Tsopano apa pali Lemba limene ine ndakhala ndiri... Lakhala likubwera kwa ine kwa zaka ndi zaka, zaka foro zapitazi. Popanda kulephera nthawi zambiri, ine ndimakhoza kutenga Baibulo, Ilo limatembenukira ku mutu uwu. Ndipo ndizo, ine sindimazidziwa izo mpaka kanthawi kapitako, zagwira ntchito mpaka ku kutseka komwe kwa Uthenga uwu usikuuno.

<sup>12</sup> Sabata yamawa ife tikhoza kudzabwereranso ku Genesis kapena kwinakwake. Ife sitikudziwa komwe ife tikupita apobe kwa sabata yamawa iyi, monga momwe Ambuye atsogolere. Koma usikuuno...

<sup>13</sup> Pamene ndinadwala kuno nthawi ina kalelo, ine sindimadwala, ine ndinali nditangosweka; ine ndinangokhala maora, ndinakhala mmizere ya pemphero, kwa masiku eyiti ndi

usiku osachokapo, osachokapo pa nsanja. Ndimadya zakudya zanga, ndi kuthana nazo zogona, pa nsanja. Ndipo ndinati, “Ine ndipempherera aliyense, ngati ine ndingakhoze kutero.” Ndipo ndikamachokapo, pamakhala anthu twente-eyiti sauzande mu mzinda ofuna kuti apemphereredwe, twente-eyiti sauzande. Chabwino, imeneyo ndi nkhani ya nyuzipepala. Iwo onse anali kumeneko, pamene nyuzipepala inati iwo anali kumeneko, *Jonesboro Sun*. Tsopano ndiye izi. . .

<sup>14</sup> [M’bale akuti, “Iwo akuyankhulabe, msonkhano umenewo uko mu Arkansas, M’bale Bill. Kulikonse kumene ine ndakhalako, kumusi uko, iwo akuyankhula, ‘msonkhano wa Branham mu Jonesboro.’”—Mkonzi]. Ife tinali ndi nthawi yopambana. Ndiko kumene akhungu, ogontha, osayankhula, olumala, ndi china chirichonse, anachiritsidwako. Zinayamba kufalikira kuchokera kumeneko kumazungulira padziko lapansi. [“Ine ndakumanapo nawo iwo. Iwo akadali ochiritsidwabe kumusi uko, M’bale Branham, kuchokera ku msonkhano umenewo.”] Ndizo zodabwitsa. Inu mukhoza kumva zimenezo, sichoncho inu? Oh, inde. Mulungu samangoika zigamba pa zinthu. Iye amachiza izo. Uko nkulondola. Iye amazipanga izo kukhala bwino. Tsopano ine ndikufuna ndidzabwerere kumusi uko ndi kukachititsa umodzi wina. Zimenezo zingadzakhale basi. . . [“Ameni. Iwo angasangalale kukhala ndi inu, iwo amabwera kuchokera konsekonse kuchokera ku mapiri ndi maenje.”]

<sup>15</sup> Ife tinalepheretsa msonkhano ku Memphis tsiku lina, kumene ife tinali ndi Mpingo wa Khristu, kapena, osati mpingo, kapena Achinyamata A Khristu ankati athandizire—Nyumba Yayikulu ya Chikumbutso mu Memphis. Ndipo Mzimu Woyera unati, “Kazibwera kunyumba,” kotero ndine ndiri pano. Ine sindikudziwa.

<sup>16</sup> Iye anali ndi Filipino mu chitsitsimutso chachikulu nthawi ina. Anamuza iye kuti apite ku chipululu ndi kukalalikira kwa mwamuna mmodzi, iye anapita kunja uko. Uko nkulondola. Anasiya chitsitsimutso, mu kutantha kwake komwe. Ndiko kulondola. Ndizo ndendende. Ife timangoyenera kuchita zimene Mulungu wanena kuti tichite.

Tsopano, ameneyo ndi Yoswa, mutu wa 1.

<sup>17</sup> Mmasomphenya opita ku India. Tsopano, inu nonse mukuidziwa nkhaniyo, pamene ine ndinabwerera kuchokera ku Afrika, ine ndinali nditakhala pambali pa bedi mmawa wina. Masomphenya amenewo. . .

<sup>18</sup> Ndi angati anayamba akhalapo mu imodzi ya misonkhano yanga ya machiritso? Tiyeni tiwone manja anu. Zedi. Inu mukuona momwe izo zimasonyezera masomphenya. Ndi angati anali pano pamene ine ndinali ndi basi—utumiki wa machiritso wa usiku kuno? Inu mukukumbukira nthawi imeneyo? Iwo anali

atadzazana paliponse kunjwa uko pabwalo, ndipo ikuvumba mvula ndi kumapitirira. Mtsikana atakulungidwa apa mu chikuku, anali akusandulika kukhala choko kuyambira mchiuno mwake kumapita mmusi, wolumala, anakhala akukhala pamenepo kwa zaka. Mzimu Woyera unamuuzwa iye zonse zimene iye anachita ndi zimene iye analephera kuchita.

Iye anati, “Ngati Mulungu andichiritse ine, ine ndikachita zimenezo.”

Ine ndinati, “Imirira, mu Dzina la Ambuye Yesu.” Ndipo apo iye anapita, kumayenda akutulukwa mchipindamo, wabwinobwino basi. Mukuona? Mukuona?

Ndicho chinthu chimene chimapeza lomwe liri vuto. Iwe umayenera kupeza vuto usanapeze mankhwala, nthawi zonse.

<sup>19</sup> Kotero ife sitikufuna kuti tiyambe pa machiritso, chifukwa, tsopano, iwe ukayamba kuyimba, *Kungo Khulupirira*, ife tikhoza kupanga mzere wa pemphero. Koma tsopano ife tikufuna kuti tiyankhule pang’ono pokha apa.

<sup>20</sup> Ndipo tsopano kuti nditsirize kukuuzani inu masomphenya awa. Ine ndinawawona iwo akutseguka pamaso panga. Ndipo Mwamuna anabwera kwa ine, iye anali ndi mapepala ena. Ndipo iye anatenga mapepala amenewo, iye anati, “Mochulukwa momwe umaganizira za chimene lidzakhale tsogolo lako,” ndipo iye anawaponya iwo monga *chomwecho*, ndipo iwo anapita mpaka mmiyamba. Ine ndinazilemba izo apa mu Baibulo. Chimodzimodzi monga ziri uko pa mwalawapangodya, ndi zimene zikanati zidzachitike mmasiku otsiriza; ndipo aliyense akudziwa chomwe izo zinali, izo zakhala basi ndendende Mawu. Izo zidzangokhala basi mwanjira iyi. Iye anati, “Tsogolo lako ndi lowala.” Ndipo iye anati, “Monga umaganizira za vuto lija limene iwe wakhala nalo, ilo lonse likusiya. Iwe sudzakhalanso nalo ilo.” Kenako iye anati, “Chinthu china,” anati, “wakhala ukudabwa za momwe ungamachitire misonkhano yako.”

<sup>21</sup> Aliyense nthawizonse ankandiuza ine, Oral Roberts amapempherera faivi handiredi pamene ine ndimapempherera awiri. Koma ine sindine Oral Roberts. Mulungu anandipatsa ine utumiki; anamupatsa Oral wina. Chirichonse chimene Oral amachita, iye amangowadutsitsa iwo ndi kusanjika manja pa iwo monga choncho. Umo ndi momwe Mulungu anamuuzira iye kuti azichitira izo. Ine ndimayenera kuyima ndi kuchiwona chinthucho mopyoza.

<sup>22</sup> Iwe umayenera kupenyetsetsa, amzanga. Ndi chinthu chowopsya. Kumbukirani, bwanji ngati Mulungu anayika themberero pa munthu kwa cholinga chinachake, kuti achite chinachake, ndiye apa nkudzabwera mneneri pamenepo ndipo nkudzachotsa themberero limenelo pa munthuyo, ndipo iwo sanachitebe izo? Ndiye iwe umakhala pa vuto ndi Mulungu.

23 Tamuyang'anani Mose, khalidwe lathu limene ife tikuliyanikhula usikuuno. Mulungu anamuza iye, "Pita uko ndipo ukayankhule kwa Thanthwe," iye anapita ndipo analikantha Thanthwe. Koma Mulungu anachita naye Mose.

24 Tamuwonani Elisha, mneneri wamng'ono uja, mnyamata wamng'ono anali wadazi. Ana aang'ono anayamba kumuseka iye, anati, "Wadazi, bwanji iwe sunapite kumeneko?" Ndipo mneneri wokwiyayo anapotoloka ndipo anawatemberera ana aang'ono amenewo, mu Dzina la Ambuye. Ndipo zimbalangondo ziwiri zazikazi zinawapha ana forte-thuu osalakwa. Tsopano, inu simungakhoze kunena kuti icho ndicho chikhaliidwe cha Mzimu Woyera. Koma iye anali mneneri wokwiya. Ndithudi. Iwe umayenera kukhala wosamalitsa.

25 Tamuwonani Yohane, nthawi ina, anati, "Kodi ife tiyitanire moto kuchokera Kumwamba ndi kuwawootcha iwo?"

Yesu anati, "Inu simukudziwa kuti ndinu mzimu wa mtundu wanji."

26 Mwaona, umayenera kukhala wosamalitsa, kumasuntha mophweka ndi pang'onopang'ono, ukupenya chimene Mzimu Woyera ukunena kuti uchite.

27 Dona wamng'ono anabwera kunyumba kuno osati kale kwambiri. Anapemphereredwa mochuluka kwambiri mpaka iye anali atadzozedwa kafifite, ine ndikuganiza. Momwe kuti chirichonse chinali chitachitika. Ine ndinali nditamupempherera iye kumeneko. Koma tinakhala pansi mchipinda mmawa wina pamene Mngelo wa Ambuye anafika pafupi, iye anayamba kuyankhula kwa iye ndi kumamuza iye basi zomwe iye anali atachita, ndi chinachake chimene iye anali kuchisunga mmoyo wake, iye anakhala nacho mmenemo kwa utali wa zaka eyiti. Iye samakhoza kumuza aliyense. Wowerenga maganizo samakhoza kuchiwona icho mwa iye. Ndipo anangotsala pang'ono kuti akomoke. Anagwera pansi ndipo anayamba kumalira. Ndipo ine ndinati, "Iwe upite ukachikonze chimenecho, ndipo Mulungu akuchiza iwe." Uko nkulondola. Iye anapita ndipo anakamutenga mwamuna wake ndipo anakakona chinthucho, ndipo anadzabworeranso. Iye wachiritsidwa lero. Ndi angati akudziwa yemwe ine ndikumukamba, mchipinda chino? Ambiri a inu mukutero, ndithudi. Ine ndikuganiza, ngati ine sindikulakwitsa, mkaziyo akhoza kukhala kuti ali pano tsopano. Chinali chinthu chochititsa manyazi kwambiri, koma Mulungu anachita ntchitoyo.

28 Tsopano, onani, kupemphera konseko, chimdidi chonsecho, kutulutsa mizimu yoyipa konseko, iye anali atasunga tchimo pansi pansu mu mtima mwake, limene iye sankafuna kuti amuwuze aliyense kuti iye anali atatero, koma Mzimu Woyera unaulula chinsinsi cha mtima wake. Iye anapita

ndipo anakakonzza zimenezo, ndiye iye anamasuka. Mulungu sadzadalitsa pamwamba pa tchimo. Inu muyenera kuzikonza zimenezo poyamba. Uko nkulondola.

<sup>29</sup> Tsopano, ndipo mu kupitirira kumeneko (M'bale Roberts), iye anandiuza ine, anati, “Monga momwe inu mukutsogoleredwera.”

<sup>30</sup> Kenako iye anandikhazika ine pansi ku Durban, South Africa, kumene ife tinali nawo anthu handiredi sauzande mu msonkhano, msonkhano wotsirizira. Tinali nawo otembenuka sarte sauzande mu tsiku limodzi, pamene iwo anawona chimene Ambuye anali atachita, momwe Iye anachitira zazikulu, ntchito zamphamvu. Ndipo apo, ndiye, ine ndinali nditakhala kumbuyo uko kachiwiri, iye anandiwonetsa ine khamu lina chimodzimodzi ngati limenelo, anandisonyeza khamu limenelo likuchokapo.

<sup>31</sup> Kenako ananditembenuzira ine mbali *iyi*, ndipo Mngelo anabwera pamenepo ndi kuwala, anadzawalitsa iko. Ine ndinangowona nyanja za anthu, ndipo iwo anali Amwenye atadzikulunga mu zovala za Chimwenye. Iye anandiuza ine, anati...Ndipo ine ndinamuwona Mngelo akubwera pafupi kwenikweni. Ndipo ine ndinati, “Kodi anthu amenewa ndi ndani?”

<sup>32</sup> Ndipo iye, Mngelo winayo amene anaimirira pafupi ndi ine, amene inu mumamuwona kumbuyo uko mu chithunzi, chabwino, iye—iye anafika pafupi ndi ine, iye anati, “Alipo firii handiredi sauzande a iwo mu msonkhano umenewo.”

<sup>33</sup> Tsopano, mulembe zimenezo mu Baibulo lanu, ndipo muwone chomwe ripotiro liri. Ndikadzabwerera kuchokera ku India, padzakhala anthu firii handiredi sauzande adzapezeke pa msonkhano kumeneko nthawi imodzi. Ine ndikuyembekezera kutembenuka kwa handiredi sauzande nthawi imodzi. Mukuona? Ndi chinthu chokhacho chimene chiti chidzathetse mafunde a Chikominisi tsopano, pamene forte peresenti ya India asanduka kale Chikominisi.

<sup>34</sup> Penyani, ngati mpingo, (ine ndikunena izi molemekeza) ngati mpingo sungathe kutulutsa zochulukira kuposa kungowerenga, kulemba, ndi masamu, ndi mbali ya maganizo ya Uthenga, Amwenye athedwa. Amwenye, monga mbadwa za ku Africa, ayenera kuti adzawone mphamvu ya Mulungu ikuwonetseredwa. Mwaona, ndakhala ndikutumiza amishonare kutali uko kwa zaka fifite, mu Afrika. Ndipo pamene omwe ankayenera kukhala Akhristu anabwera, iwo anali atanyamula fano laling'ono lamatope mu nkhwapa mwawo, bwanji, mmishonare anawauza iwo...Bwanji, za machiritso, iwo amapeza machiritso kuchokera mu fanolo, (osati kudzera mwa fano) kudzera mwa Mulungu, Mulungu anatsinzina pa umbuli wawo. Koma pamene zinafika pa malo amene iwo anali oti achiritsidwe,

mmishonareyo anati, “Oh, zinthu zimenezo, masiku ake anatha. Ife tiri nazo izo mu seminare. Mwaona, izo zinadutsa kale. Palibepo chinthu chonga choterocho.” Chabwino, iye ankanyamula fano lake pofuna machiritso.

<sup>35</sup> Ine ndinamuza iye kuti Mulungu yemweyo amene mmishonare ankamukamba, anali Mutu wa machiritso onse, ndipo anatsimikizira izo kwa iwo pa nsanja, zitatero iwo anamulandira Khristu ndipo anapita mu nkhalango ndi kumeneko. Mmodzi wa anyamata kunja uko, amene anapita kumeneko, akumabatiza pafupifupi sauzande pa sabata, pakali pano, nzika zenizeni. Imeneyo ndi mishonare. Mulungu akuchita ntchito yofulumira kwenikweni.

<sup>36</sup> Ndi angati anamvapo *The Wings Of Healing*, Dokotala Wyatt ndi iwo; ndi mzanga wa pamtima wanga, Raymond Hoekstra? Zoona, iye walalikirapo pomwe pano pa kachisi, Raymond Hoekstra. Iye anapita ku East India, kumtunda uko, ndipo anali ndi chitsitsimutso, ndipo anali ndi masauzande a otembenuka kumtunda kumeneko. Mukuona chimene Mulungu akuchita? Oh, oh, taonani, pali. . .

<sup>37</sup> Ndiroleni ine ndifunse, ndinene izi. Ndiroleni ine ndikupatseni inu kufotokozera kwake. Apa, *pali* gawo limodzi, *apa* pali gawo lina, ndipo *apa* pali linanso. Tsopano, pansi *apa* pali mpingo wadzina lokha; tsopano pamwamba *apa*, apa pali chopambana, apa ndi pamene ife tikuyenera kukhalapo, khomo loyandikana nalo la Kumwamba, kumene Mphamvu za Mulungu zikutsikira pansi. Chabwino, Izo zikugwera pa *ichi*, zikugwera pansi kumadutsa kwa *ichi*, kenako kutsika mpaka ku chimodzi *ichi*. *Uwu* ndi mpingo wadzina lokha, iwo ukungopitirira, basi pa kudzinenera kozizira ndi—ndi kachitidwe kakang’ono kamwambo, umenewo ndi mpingo wadzina lokha, iwo amangodontha pang’ono; mpingo wotsatira, kumtunda *kuno*, Uthenga Wathunthu, umalandira ena a madalitso, koma iwo amapita mu timalingaliro; ngati ife tiyenera kuti tikweze mmwamba mu gawo lotsatira ili *apa* ife tisanakhale konse ndi Mkwatulo, ndendende kulondola, inu muyenera kuti mukwere mu Izo ife tisanakhale nazo izo. Ndipo izo nzoona.

<sup>38</sup> Tsopano, ndipo inu—inu mulembe izo mu Baibulo lanu. Iye sanayambe wandiuzapo ine kalikonse, ayi nkomwe kuyambira pamene ine ndinali khanda, ndipo Lawi la Moto lija. . . Ndipo amayi anga omwe akhala kumbuyo uko tsopano, usinkhu wa zaka fiftini pamene ine ndinkabadwa, iye anatsigula zenera laling’ono, ndipo Mngelo wa Ambuye anabwera mmenemo ndipo anadzayima pamenepo. Kutu, kuyambira nthawi imeneyo, kuyambira pamene ine ndingakhoze kukumbukira, sanayambe wandiuzapo ine chinthu chimodzi chimene chiri cholakwika. Ndipo ndine pano mu mzindawu kumene ine ndinabadwirako ndi kuleredwa. Ena a inu nonse, alendo, fufuzani pozungulira

kudutsa mzindawu, ndipo mumufunse munthu aliyense ngati chinthu chimodzi chinayamba chanenedwapo mu Dzina la Ambuye koma chimene chinafika pochitika ndendende basi monga Iwo ananenera. Kotero ine ndikudziwa Izo ziri bwino, mwaona, Ndi Mulungu.

<sup>39</sup> Tsopano, ndipo pa mapeto a zimenezo, mapeto a masomphenya amenewo, ine ndinawona Baibulo langa likubwera kwa ine, ndipo Ilo linadzatzsegula ku Yoswa 1. Ndipo zimenezo zakhala nthawizonse pamaso panga. Oh, basi, ine ndimalephera kuti ndichoke kwa zimenezo.

<sup>40</sup> Ndipo usikuuno ine ndikufuna kuti ndiwerenge izo, chifukwa ndizo kuwatenga ana a Israeli; Yoswa, mtsogoleri wamkulu. Ndiye ife tidzabwereranso ku Numeri ndi kukatenga phunziro lathu, ndi kutuluka nalo ilo mu mphindi twente kapena sarte zotsatirazi, kapena chinachake chonga icho. Ife tikhala ndi utumiki wa ubatizo, ndipo kuti ife timupange iye. . . inu mukhoza kumakonzekera zimenezo.

<sup>41</sup> Tsopano mvetserani mwatcheru pamene ife tikuwerenga Yoswa 1. Itachitika imfa ya Mose, ndi pamene ife tinasiyira izo usiku wathawu. Ndi kulondola uko? Mose, kodi ife tinamusiya pati Mose? Ataima paphiri, akuwatsanzika anthu ake. Ndipo iye anali woti akukafa, atagona pamenepo. Ndipo iye anayang'ana, ndipo apa panayima Thanthwe litaima pafupi ndi iye. Iye basi anangoonda pa Thanthwelo, ndipo Angelo anabwera, kudzamutengera iye kutali.

Chabwino, *itachitika imfa ya Mose mtumiki wa AMBUYE zinafika pochitika, kuti AMBUYE anayankhula kwa Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Mose, . . .*

*Mose wantchito wanga wafa; tsopano chotero nyamuka, ndipo muwoloke Yordano uyu, iwe, ndi anthu onse, kulowa mukalowe mdziko limene Ine ndidzapereka kwa iwo, ngakhale kwa ana a Israeli.*

*Malo aliwonse. . . zidendene za mapazi anu zidzapondapo, amenewo Ine ndapereka kwa inu, monga Ine ndinanena kwa Mose.*

*Kuyambira ku chipululu ndipo mpaka ku Lebanoni uyu ngakhale mpaka waukulu. . . mtsinje wa Firate, mayiko onse a Ahiti, kufikira kunyanja yaikulu kumka kulowa kwa dzuwa, kumeneko kudzakhala malire anu.*

*Sipadzakhala pali munthu aliyense adzathe kuima pamaso pako masiku onse a moyo wako: monga Ine ndinali ndi Mose, momwemonso Ine ndidzakhala ndi iwe: Ine sikuti ndidzakusiya iwe ngakhale kukulephera iwe, kapena kukulephera iwe, kapena kukusiya iwe.*

*Khala wamphamvu ndi wolimbika bwino: pakuti kwa anthu awa iwe udzagawa cholowa dzikoli, chimene*

*Ine ndinalumbirira makolo awo kuti ndidzapereka kwa iwo.*

*Ungokhala...wamphamvu ndi wolimba mtima kwambiri, kuti usamalire kuchita...malamulo onse amene Mose wantchito wanga anakulamulirani inu: usatembenuke kuchoka ku dzanja lamanja kapena kulamanzere, kuti iwe ukapindule kulikonse kumene upitako.*

*Bukhu ili la chilamulo lisachoke pakamwa pako; koma iwe uzilisinkhasinkha usana ndi usiku, kuchitira kuti uzisamalira kuchita monga mwa zonse zalembedwa mmenemo: pakuti potero iwe udzapangitsa njira yako kupindula, ...ndiye iwe udzachita bwino.*

*Kodi Ine sindinakulamulire iwe? Khala wamphamvu ndi wolimbika mtima; usachite mantha, ngakhale kukhala...wokhumudwa: pakuti AMBUYE Mulungu wako ali ndi iwe kulikonse kumene upitako.*

<sup>42</sup> Tsopano, ife tibwerera mmbuyo tsopano ku Bukhu la Numeri, ndi kupitiriza pamene ife tinasiyira usiku wathawu.

<sup>43</sup> Tsopano ine ndikufuna tcheru chanu chosagawanika, kwa maminiti pang'ono chabe, chifukwa inu mwadzazana. Ndi ambiri aimirira, ndi zina zotero, ndipo ife tikupepesa pa izi, koma ife sitingakhoze kudziletsa izo, kachisi si wamkulu. Tsopano ife tinamusiya Mose...

<sup>44</sup> Ana a Israeli anali atatuluka kuchokera mu Igupto. Iwo anakalowa mu chipululu, anayamba kung'ung'udza. Mulungu anatumiza njoka zamoto pakati pawo ndipo zinawaluma iwo, iwo anali akufa, mwa masauzande. Ndiyeno Iye anapanga chitetezero, njoka yamkuwa. Oh, zokongola bwanji! *Njoka yamkuwa* ija, kuyankhula za chiweruzo, "chiweruzo Chaumulungu, ndi tchimo loweruzidwa kale." Genesis 3:14, Mulungu anali ataweruzo kale njoka. Ndiyeno mu Eksodo 17, ife tikupeza kuti mkuwa umayankhula za chiweruzo Chaumulungu, guwa lamkuwa. Ndiye, aponso, mmasiku a Eliya, ife tinapeza kuti milengalenga munali mwa mkuwa. Mkuwa nthawizonse ndi chizindikiro cha chiweruzo Chaumulungu.

<sup>45</sup> Usikuuno, mafuko akukhala amkuwa; chiphiphiritso, chiweruzo chiri pafupi. Ine ndikukhulupirira ife tikukhala mu kutsekera kwa mbiriyakale ya dziko lapansi. Ine ndikukhulupirira kuti chiweruzo Chaumulungu chiri pa mafuko, ndipo Mulungu wazilola zinthu izi. Chifukwa ife tinanyalanyaza Khristu, ndi chifukwa chake Chikominisi chinasesa maiko. Ife tatenga masauzande a nkhumba ndi kuzipha izo, ndi kuziwotcha izo kunjira kuno pa minda. Ife sitinakhoze kuyenda kanjira, kowongoka kopapatiza. Ife tinabweretsanso akachasu ndi mowa. Ife tinawotcha tirigu, nkumugalauzira iye pansu. Tinalitaya thonje; ndipo mahandiredi

a ana aang'ono azizidwa mpaka kufa, pafupifupi, mu chaka. Chabwino, ife tiri nazo izo tsopano, Chikominisi chinadzasesa mkati momwe ndi kuzichotsa izo kumapazi.

<sup>46</sup> Nzosadabwitsa kuti Chikhristu sichikukhoza nkomwe kukweza muyezo, ndi chifukwa, osati chifukwa Khristu sangakwanitse, koma chifukwa chakuti anthu sangakhoze kuchita zimenezo. Uthenga wakonzeka, Mphamvu ya Mulungu ndi yokwanira. Amuna ndi akazi akuwopa kutulukira kutsidya mmadera amenewo pamaso pa Mulungu, ndipo akuwopa kuti amudalire Iye, kutenga Mawu Ake.

<sup>47</sup> Mose, ndiye iye analephera Mulungu. Mose ndi choyimira changwiwo cha bungwe la mpingo. Ndizo, mundikhululukire ichi, abale, koma ine ndikufuna inu mumvetsere mwacheru. Zinthu zonsezo zinali mthunzi ndi choyimira.

<sup>48</sup> Ndipo lero mukumamva anthu akunena kuti, “Oh, ine ndine *Wakuti-ndi-wakuti*. Ndine wa Methodisti.” Osati zokhazo, koma anthu Achipentekoste, anthu achiyero, “Ndine wa Assemblies, iwo ndi akulu kwambiri! Ndine wa Mpingo wa Mulungu.” Mulungu samasamala mochuluka *chomwecho* za chimodzi cha izo, kapena aliyense wa iwo. [M'bale Branham anakhwatsitsa zala zake—Mkonzi]. Ayi, bwana. Mulungu amakhala ndi chidwi ndi munthu payekha, ndipo mwamuna aliyense kapena mkazi amene angayesere kumukhulupirira Iye.

<sup>49</sup> Mose anali choyimira cha bungwe la mpingo, chimene, iye anali lamulo. Ndipo Mose anadzipsa yekha ulemelero pamaso pa anthu, mmalo molemekeza Mulungu. Ndipo Mulungu anatembenuka kumuchokera iye.

<sup>50</sup> Ndipo lero mpingo wayamba kudzipatsa ulemelero wokha mmalo molemekeza Mulungu. Iwo akuyesetsa kukhala ndi mamembala ochuluka, matchalitchi abwinoko, malimba abwinoko ndi mipando yabwinoko, ndi tchalitchi chachikulu. Mulungu sapereka zochuluka *chotero* kwa izo. [M'bale Branham anakhwatsitsa zala zake—Mkonzi]. Inu muyenera kumamukweza Mulungu. Ine kulibwino ndikhale ndi mishoni yakale yaing'ono kwinakwake, yosedwawo, uko ku Bowery penapake, kumene iwo angakhoze kumasuka kwenikweni ndi kumafuula, ndi kumamutamanda Mulungu ndi kumakhala ndi nthawi yabwino, kuposa ma cathedral onse akuluakulu padziko lapansi. Amen. Uko nkulondola. Mulungu wathana nayo mibadwo ya mpingo.

<sup>51</sup> Tsopano zindikirani, Iye anamutsutsa Mose chifukwa Mose anadzipsa ulemelero yekha.

<sup>52</sup> Ndipo inu mungopenya lero. Mipingo ikuluikulu iyi, iyo yonse ikufuna kuti inu mubwere ku tchalitchi chawo ndi bungwe lawo. Ndipo mlaliki aliyense akukokera kuyesetsa kuti asomeke nthenga mu chipewa chake, iye azipitirira nazo, kumati, “Chabwino, ine ndikhoza kukhala mkulu wachigawo.

Ine ndikhoza kukhala *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*.” M’bale, ine ndikufuna kuti ndikhale Mkhristu. Ndicho chimene amuna ndi akazi akusowa, ndi Khristu. Oh, pamene ine ndiyamba kuwawona iwo, kuwona momwe iwo akuchitira!

<sup>53</sup> Izo zikundikumbutsa ine kuno osati kale litali, ine ndinali pa ka—katchuthi kakang’ono ine nditabwerera kuchokera ku Africa. Ine ndinali kumtunda kuno mu nkhalango ya kumpoto, kutali komwe kuno kumalire a Alaska, mailosi sauzande kuchokera ku msewu wa tara. Ndinabwerera mmbuyo masiku sikisi, pa nsana wa kavalo, ndikupita kutali ndi chirichonse. Ndipo pamene ine ndimabwerera kudutsa kumeneko, ine ndinali kukwera pa kavalo wanga, tsiku lina, ndipo iye anangochita mantha. Chimbalangondo chotuwa chinangowuka, ndipo iye anachita mantha. Ndipo ine ndinali kupita kudutsa, kapena iye anayamba kuthamanga, ndipo ife tinakafika kumusi kudutsa kumeneko. Ndipo apo panali kuwotchedwa kwachikale, ndipo apo panali gulu lalikulu kwambiri la mitengo ikuluikulu yachikale yaitali imene inayima pamenepo. Ndipo iyo inali yoyera, apo mu kuwala kwa mwezi, oh, basi molemekezeka ndi mwamphamvu monga iwo ankawoneka kuti ali. Moyo wonse unali utachoka mwa iwo. Ndipo ine ndinamvetsera ku mphepo ikuwomba, ndipo mphepo inabwera kudzatsika kudutsa pamenepo, ikungobuula, inu mukudziwa, ndipo mitengo yakale yonseyo zonse zomwe ikanachita ndi kulira ndi kukuwa, ndi kulira ndi kukuwa.

<sup>54</sup> Uko mu Yoweli, Ilo linati, “Chimene chimbalinga chinasiya, anoni anadzadya; chimene anoni anasiya, mbozi yapani inadya.” Mipingo imeneyo, oh, mosakaika, chimodzimidzi monga mitengo imeneyo, iyo nthawiyina inali zoimikidwa zazikulu zamoyo, Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste. Koma ine ndikukuuzani inu, moto ndi zowotcha za—za dziko lapansi zawotcha khungwa lonse kuchoka pa iwo, iwo akuima ngati mulu waukulu wa miyala ya pamanda tsopano, ndipo basi angoyimitsidwa pamwamba apo, mulibe Moyo mwa iwo nkomwe. Amen. Uko nkulondola. Ndipo pamene mphepo yamkokomo yamphamvu ibwera kuchokera Kumwamba, pansu, chinthu chokhacho chimene iwo amachita ndi kulira, ndi kukuwa, ndi kubuula, ndi kumayankhula motsutsa izo. Aleluya! Chimene ife tikusowa ndi winawake kuti avomereze izo!

<sup>55</sup> Ndipo ine ndinazindikira kumusi uko, mitengo yaing’ono iyo yomwe inali kubwera, iyo inali yomasuka, iyo imangoperekera ku mphepo, kubwerera mmbuyo ndi mtsogolo monga *chonchi*, kumakhala ndi nthawi yabwino. Ine ndinati, “Izo zikundiyika ine mmalingaliro a chitsitsimutso chabwino, cha kachitidwe-kachikale, chotumizidwa ndi Mulungu, cha Mzimu Woyera.” Aleluya!

<sup>56</sup> Pamene zizindikiro ndi zodabwitsa zinayamba kumabwera mu tchalitchi, mipingo ikuluikulu yakale ikulira, “Ine

sindimakhulupirira mu zinthu zimenezo. Kumeneko ndi kutengeka. Masiku a zozizwitsa anapita.” Ndipo Mphepo ikuyimba mluzu mmusi momwe, zomwewo zimene zinawapangitsa iwo kulira, zinawapangitsa enawo kusangalala. Aleluya!

<sup>57</sup> Ndipo pamene muwugwedeza mtengo umenewo, nthawi iliyonse iwo ukagwedezeka, iwo umamasula mizu kuchitira kuti ukule nkumapita pansi kukapeza kugwira kwabwino. Aleluya! Ndicho chimene ife tikusowa usikuuno, ndi kugwedeza kwabwino, kwanthawi-yachikale, kwa Mzimu Woyera, komafika pansi (Ulemelero kwa Mulungu!), kupeza kugwira kwa kachitidwe-kachikale pa Mulungu. Kugwedeza konse ndi kukoka kumene Mzimu Woyera umakuchitirani inu, Iye amamasula zonyansa pozungulira mizu kuti Iye akhoze kukumba pansi, mupeze kugwira kwabwinoko, muzike mizu bwino ndi kukhazikika mwa Khristu Yesu, ndi zokuchitikirani zina: chokuchitikirani cha machiritso; chokuchitikirani cha ubatizo, Mzimu Woyera; chokuchitikirani cha mphatso za Mzimu. Aleluya! Chimangokuzikikani inu mwa Khristu, mwamphamvu pamene chikuwomba!

<sup>58</sup> Usiyeni mpingo uzilira ndi kumabuula ngati iwo ukufuna kutero. Usiyeni iwo uziti, “Masiku a zozizwitsa anapita,” ngati iwo akufuna kutero. Iwo anafa, mulimonse. Oh, iwo amati, “Ndife mpingo!” Chomwechonso iyo inali, mitengoyo.

<sup>59</sup> Koma, tayang’anani pa iwo. Panalibe khungwa pa iwo, matuza chabe, khungwa lonse linali litapsya. Iwo sakanakhoza kunyamula moyo, ndicho chifukwa chake. Ngati mitengo imeneyo ikanakhala ndi khungwa pa iyo, ndipo iyo nkumakhoza kunyamula moyo mwa iyo, iyo ikanakhalanso moyo. Koma khungwa lonse, iwo anapita kale kumeneko ndipo anakapanga miyambo yawo ndi zina zotero, kotero iwo sangakhoze ngakhale kukhala ndi khungwa lirilonse pa iwo, palibe kanthu koma kumangolira ndi kufuula pamene mphepo zikuwomba.

<sup>60</sup> Koma Mulungu anatuziza Mphepo mofanana basi. Kotero, mpingo wawung’ono kwambiri uwu ukubwera, wodzaza mdzanja, iwo anali akungokhala ndi nthawi yopambana nayo Iyo, pamene ena onsewo anali akutengeka nazo izo. Oh, mai! Ife tikusowa mphamvu ya Mulungu mu mpingo!

<sup>61</sup> Tsopano, pamene iwo anachoka, Mose akufa, iwo anayamba kupita cha ku dziko lolonjezedwa. Tiyenera kuti tifulumire tsopano chifukwa ife tiribe nthawi yochuluka kwambiri.

<sup>62</sup> Koma iwo anayamba kupita cha ku dziko lolonjezedwa, ndani anabwera mu njira yawo? Koma tsiku lina kunali mfumu yachikulire yomwe inakondwera kwambiri ndi gulu ili la Ahebri likubwera kumadutsa kumeneko. Ndipo iwo ankadziwa kuti Mulungu anali ndi iwo. Kotero iye anapita uko ndipo anakatenga mneneri kuti abwere ndi kudzawatemberera iwo,

dzina lake Balaki. Ndipo Balaamu wakaleyo analandira... Balaki anali ndi mneneri dzina lake Balaamu. Ndipo Balaamu anakwera pa bulu wamng'ono wakale, Iye (Mulungu) atatha kumuuzza iye kuti asapiteko. Ndipo, inu mukudziwa, iye anayamba kumatsika akudutsa, atakwera bulu wake, ndi antchito angapo. Iye anali akupita kukatemberera Israeli. "Zedi, ine ndipita ndikasamalira gulu ilo la oyera odzigudubuza mmalo mwanu. Ine ndikawakonzaza iwo." Kotero iye anakwera pa bulu ndipo anapita kumeneko, mpaka kudutsa kumeneko. Chinthu choyamba inu mukudziwa...

<sup>63</sup> Bulu anali ndi kupenya kwauzimu kochulukira kuposa momwe mlaliki anali nako. Uko nkulondola. Bulu anawona Mzimu Woyera utayima panjira, ndi lupanga losolodwa. Iye anathamangira mmunda, anamphwanyitsira mlaliki wakaleyo phazi lake. M'bale, chimene ife tikusowa lero ndi kukwera bulu winanso. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Uko nkulondola. Inde, apo iye anabwera. Iye anathamangira mmunda, iye anamuwona Mngelo wa Ambuye atayima panjira.

<sup>64</sup> Ndipo kotero nthawi yotsatira, Iye (Mzimu Woyera, Woyera) unapita mu kanjira kakang'ono, ndipo unadzayima pamene kachiwiri. Ndiyeno chinthu choyamba inu mukudziwa, anayamba kumukoka bulu wakaleyo ndi kumayesetsa kuti amupangitse iye azipita, ndipo buluyo anangogona pansu pomwepo. Iye anayamba kumugonyuza iye, ndi kumamumenya iye ndi ndodo, ndipo buluyo anatembenuka ndipo anayankhula ndi liwu la munthu, ndipo anati, "Kodi ine sindinakutumikireni inu bwino mu zinthu zonse izi?" Ndipo mneneriyo apobe anali wokwiya kwambiri, sanazindikire nkomwe zomwe buluyo anali kunena. Oh, mai!

<sup>65</sup> Ngati Mulungu angagwiritse ntchito lirime la bulu wosayankhula, kuti ayankhule, ndithudi Iye akhoza kugwiritsa ntchito mwamuna kapena mkazi yemwe angadzipereke yekha kwa Mulungu. Aleluya!

<sup>66</sup> Ndipo tsopano, ndiye chinthu choyambirira, mamba anakang'anuka kuchokera m'maso mwa mlalikiyo, ndipo iye anayang'ana pamene ndipo anawona lomwe linali vuto. Pamene panayima Mzimu Woyera, kapena Mngelo wa Ambuye, pa njirapo.

<sup>67</sup> Iye anapita kumeneko, ndipo iye ankaganiza kuti ndithudi iye akanawatemberera anthu amenewo. Kotero pamene anapita kumeneko, ife tikupeza chithunzi chabwino cha izo apa mu Yuda, ngati tingatembenezire kumeneko. Mvetserani. Pamene iye anakafika kumeneko, iye anati... Tsopano penyani Balaamu. Ndipo Balaki adzamuwonetsa Balaamu Israeli, kotero iye akupita ndipo akukamanga guwa lake. Iye anali mneneri, Balaamu anali. Kotero iye anangomuwonetsa iye gawo la Israeli, gawo loyipitsitsa basi.

<sup>68</sup> Ndipo ndizo ndendende basi momwe mdierekezi akuchitira lero, iye amangokuwonetsani inu gawo loyipitsitsa la chinthucho. Ndicho chimene mdierekezi amawawonetsa ena a azilaliki amakono awa a zafioloje, kungoti, “Tsopano, taonani apa, inu mukumudziwa John Doe, yemwe ankakhala cha kuno, iye anathawa ndi mkazi wa *Wakuti-ndi-wakuti*. Ife takhala nazo zokwanira za gulu ilo la oyera-odzigudubuza.” Iye sanaganizire za ena mu gulu lake lomwe omwe ankachita chinthu chomwecho. Uko nkulondola. Koma iwo akhoza kuziphimba izo.

<sup>69</sup> Koma, mvetserani, iye anamuwonetsa iye zochuluka *kwambiri* basi za Israeli, ndiye iye anamutengera iye mmbuyo ndipo anakamuwonetsa iye zochuluka kwambiri *apa*. Koma pamene iye anafika kumaloko, ndipo Balaamu, iye anaganiza, “Ndithudi ngati Israeli wachita cholakwika...” Iwo achita cholakwika. Iwo anali atachita chirichonse mu kalendala ya Mulungu, cholakwika, pafupifupi. Koma chiyani, ndipo Balaamu anaganiza kuti Mulungu woyera ndithudi akanawatemberera anthu amene anali atachita cholakwika zochuluka choterocho. Iye anaganiza, “Ndithudi Mulungu adzachita zimenezo.” Kotero pamene iye anafika kumeneko, iye anali atapenga nazo kwambiri ndalama mpaka iye samakhoza kuchiwona chifukwa chimene Mulungu sanali kuwatemberera iwo. Ndipo nthawi iliyonse iye akayesera kuti awatemberere iwo, iye amawadalitsa iwo. Iye amakhoza kuponyera uneneri wake monga chomwecho, ndi kupita patsogolo ndi kukatenga chovala chake ndi fanizo lake; ndipo mmalo motemberera, ilo limakhala dalitso likugwera mobwerera kwa iwo, “Mahema ako ndi olungama bwanji, O Israeli,” momwe iwo analiri akulu. Mmalo motemberera, ilo limakhala dalitso.

<sup>70</sup> Zomwe Balamu analephera kuti aziwone, ndi zomwe alaliki amakono ndi anthu amakono akulephera kuti aziwone mu Mpingo wa Mzimu Woyera lero. Iwo amati, “Ine ndikudziwa ambiri a iwo amadzitcha okha *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*, ndipo zinthu zambiri zomwe iwo azichita.” Ine ndikuvomereza zimenezo, m’bale. Iwo amati, “Iwo amazichemerera ndi *ichi*, ndipo iwo achita *icho*, ndipo achita *ichi*.” Izo nzoona, ine ndikuvomereza kuti iwo achita zolakwika.

<sup>71</sup> Koma pamene Balaamu analephera, kuti awone Njoka Yamkuwa ija ndi Thanthwe lokanthidwa lija likupita patsogolo pa Israeli, likupanga chitetezero. Uko kunali kuyitana kwa Mulungu, kusankha kwa Mulungu. Iwo anali anthu a Mulungu. Aleluya! Mulungu anali atawayitana iwo ndipo anawalekanitsa iwo, ndipo anayika Njoka patsogolo pawo (ngati chitetezero) ndi Thanthwe lokanthidwa, ndipo Balaamu analephera kuti awone Zimenezo. Mu tsiku limene mlaliki wamakono akulephera kuwona mphamvu ya Mzimu Woyera, Yesu Khristu wokanthidwa, kuti ife tiri mu Thupi Lake, mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi

limodzi ndi kukhala ziwalo za Thupi limenelo. Ndipo ndicho chimene munthu wamakono analephera kuchiwona mmenemo. Mpingo wa Mzimu Woyera umenewo usanapite patsogolo, iwo akulephera kuti awone zimenezo, Thanthwe lokanthidwa lija, Njoka Yamkuwa ija ikupita patsogolo pa mpingo, ikupanga chitetezero. Balaamu analephera kuziwona Zimenezo.

<sup>72</sup> Ndiye pamene Yoswa anatsikira ku mapeto, Yoswa anatenga malo a Mose. Yoswa anali ali mu msasa nthawi zonse. Iye ndi Kalebu anali awiri okhawa amene anayamba kumbuyo uko pachiyambi, amene anawolokera kumeneko. Tsopano m'badwo wonsewo unafa chifukwa cha kusakhulupirira. Mulungu anawuyamba m'badwo watsopano, Iye anayamba ndi Yoswa kuti akhale mtsogolero, iye ndi Kalebu.

<sup>73</sup> Tsopano zindikirani, monga mpingo walephera. Chinthu chomwe chakhala chiri mu mpingo nthawi zonse, komabe osazindikirika, mphatso za Mzimu, mawonetseredwe a Mzimu, ndi zomwe zikuwunyamula mpingo tsopano ndi kumayenda chitsogolo.

<sup>74</sup> Tayang'anani mmasiku akale kumbuyo uko, iwo, iwo ankamanga mahema awo. Panali Lawi la Moto lomwe linkawatsogolera iwo. Ndipo nthawi iliyonse Lawi la Moto limenelo likasuntha, iwo ankasuntha nalo Ilo. Ilo linkakhala pamwamba pa mahema. Ndipo ngati iyo ili teni koloko usiku, thuu koloko madzulo, apo pamakhala malipenga sauzande amaphulitsidwa pakamodzi; mu Israeli aliyense amatsitsa hema wake, nazula zikhomo zake, ndipo amayalula chirichonse, ndipo iwo ankatsatira Lawi la Moto.

<sup>75</sup> Oh, chimenecho chikanakhala chinthu chabwino lero! Iwo ankatsatira Lawi la Moto. Ndiyeno pamene Lawi la Moto layima, iwo ankamanga pansu pake. Zimenezo zinatayika kwa mpingo.

<sup>76</sup> Mmasiku a Martin Luther, atatha faivi...zaka mazana fikitini handiredi za mibadwo ya mdima, Martin Luther anawona Lawi la Moto likuyenda, ndipo iye anatuluka kuchokera mu Mpingo wa Katolika, ndipo iye ankatsatira Lawi la Moto ndipo anawatulutsa teni sauzande a iwo.

<sup>77</sup> Ndipo kenako Martin Luther anamanga pansu pa Lawi la Moto. Ndipo pamene iye anakafika kumeneko, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye anapanga bungwe lalikulu lotchedwa mpingo wa Chilutera. Koma tsiku lina Lawi la Moto linayamba kusuntha kachiwiri, koma Martin Luther sankakhoza kusuntha, chifukwa iye anachita bungwe. Iye ankayenera kukhala pamenepo. Uko nkulondola.

<sup>78</sup> Ndipo munthu wamng'ono uko mu England, dzina lake John Wesley, analiwona Ilo. (Ndipo Martin Luther ankati, "Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro.") Ndipo tsopano, ndipo John Wesley ananena kuti, "Yesu anazunzika kunja kwa zipata, kuti Iye akakhoze kuwayeretsa anthu ndi Magazi Ake Omwe."

Iye anawona kuyeretsewa. Lawi la Moto linasuntha, koma Luther sanathe kusuntha, chifukwa iye anachita bungwe.

<sup>79</sup> Ndiroleni ine ndinene izi kwa inu, m'bale. Mulungu, mu Baibulo Lake, analibe konse mpingo wa bungwe. Ndicho Chiphunzitso. Mpingo wa Katolika umati iwo ndi “manthu wa mpingo.” Iwo *ndi* manthu wa mpingo. Iwo ndi manthu wa mabungwe, ndipo Chivumbulutso 17 amanena chinthu chomwecho. Uko nkulondola. Iwo ndi mpingo woyambirira wa bungwe. Ndipo iyi yangokhala basi yaying'ono—ana aakazi aang'ono amene achokera kumeneko, kawerengeni Chivumbulutso 17. Ife tifika mu zimenezo sabata yamawa. Chabwino, zindikirani.

<sup>80</sup> Ndiye iwo sanakhoze kusuntha, kotero John Wesley anawona Lawi la Moto ndipo iye anasuntha kumatsatira Ilo. Ndipo iye anakoka aakulu. . .Iye anapulumutsa mafuko. Pafupifupi mafuko atatu kapena foro anali mu kuvunda kwa khalidwe, ndipo John Wesley anawona Lawi la Moto ndipo anayambitsa chitsitsimutso cha Wesley chimene chinasesa kuzungulira dziko, ndipo anabwera cha kuno, iye ndi Asbury ndi iwo, ndipo anapulumutsa tsikulo. Uko nkulondola.

<sup>81</sup> Ndiyeno chinthu choyamba inu mukudziwa, John Wesley atapanga bungwe mwakathithi, Lawi la Moto linayamba kusuntha kenanso. Wesley sanakhoze kusuntha, chifukwa iye anachita bungwe. Ndipo anthu Achipentekoste analiwa Ilo, ndipo kumeneko iwo analitsatira. Ndi zoonza zimenezo, anamusiya Wesley atakhala mu mthunzi; Mulungu anakamuika iye pa alumali ndi Luther. Chabwino. Tsopano, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iwo anali ndi chitsitsimutso chachikulu, chitsitsimutso cha Chipentekoste, kubwezeretsa kwa mphatso ndi zina zotero.

<sup>82</sup> Ndipo tsopano, chinthu choyambirira inu mukudziwa, Lawi la Moto layamba kusuntha kenanso. Koma Pentekosite yachita bungwe kwambiri, iyo siyingakhoze kupita. M'bale, iyo zinapweteka, sichoncho izo. Ndipo ndizo zabwino. Iyo yachita bungwe kwambiri, kukhuthala mpaka iyo siyingakhoze kusuntha. Uko nkulondola. Izo nzoona. Koma Lawi la Moto likuchokapo, m'bale, ndipo pali anthu amene akupita nalo Ilo. Aleluya! Ife tikupita ku Dziko lonjezedwa! Inde, bwana.

<sup>83</sup> Pamene Mose analephera, Yoswa anawona Lawi la Moto lija likusuntha, anati, “Bwerani, ana, ife tiri panjira yathu.” Iye anawatengera iwo kumeneko ku tsidya la Yordano. Oh, pamene ine ndiganiza za zimenezo, ndi zokongola bwanji! Iye anati, “Tsopano, ife tisanawoloke, ife tilola azondi angapo kuti achepere. . . asambire kumeneko.”

<sup>84</sup> Inu mukudziwa nkhani ya hule, Rahabu, Rahabu hule, kani, momwe iye anatsitsira zovala zofiirazo, ndipo anapulumutsa nyumba yake. Mwa chikhulupiriro, iye anapulumutsa tsikulo,

iyе anapulumsа iyе ndi apabanja аke. Makoma onse anagwa kupatula gawo lake, chifukwa panali mlozo wofiira pa chitseko chake.

<sup>85</sup> Monga ife tinali nazo usiku wina, mngelo wa imfa akudutsa. Kodi pali chingwe chofiira pachitseko chanu kugwedeza kwakukulu uku kusanachitike? Iye anati, “Sikuti kamodzi kenansо Ine ndidzagwedeza dziko lapansi, koma Ine ndidzagwedeza miyamba. Ndipo ife tidzalandira mphamvu ya Ufumu umene sungakhoze kugwedezeka,” Ahebri. Uko nkulondola. Ife tikukhala mu ora limenelo! Tsopano penyani.

<sup>86</sup> Ine ndikumuwona Yoswa, mtsogoleri wachichepere. Mulungu akukumana naye iye, Iye anati, “Usachite mantha tsopano, iwe. Mose wantchito wanga wafa, koma nyamuka ndipo uwoloke Yordano uyu. Palibe munthu, masiku onse a moyo wako, adzakhoze kuyima pamaso pako. Monga Ine ndinali ndi Mose, chomwechonso Ine ndidzakhala ndi iwe. Usawope ayi, ukhale wamphamvu ndi wolimbika mtima ndithu.” Mai, ine ndikukhoza kumuwona wankhondo wakale uja akuyenda pamene, munthu wachichepere wodzichepetsa. Iye anali mkati. . . Iye anali ataitanira Israeli yense pamwamba limodzi, ndipo ankayang’ana pansi kutsidya kwa Yordano uko. Munalі mu mwezi wokolola, Epulo. Ndiyeno chipale chofewa chinali chitasungunuka mu Yudeya, ndipo uko kunali mtsinje wawukulu ukubwera chotsika kumadutsa kumeneko, ukubangula.

<sup>87</sup> Ine ndiri, ine ndinakuuzani inu ife tiri ndi kanema wa zimenezo pamene abale athu ena anali cha uko kuno posachedwapa, ndipo iwo anali ndi msonkhano kumeneko, kapena amangodutsa, kukonzekera, ine ndikupitako ku msonkhano. Ndipo analipo pafupifupi forte a iwo. Ndipo anafika pa malo amenewo, ndipo iwo anakuwa ndipo anakhala ngati akugwetsera pansi tchire lonselo kuzungulira kumeneko. Ndipo pamene iwo anafika kumeneko, kumene Yesu anabatizidwa kumtunda uko ndi Yohane, mmodzi aliyense wa iwo anayamba kukuwa, analumphira mmodzi ndi kubatizidwa wina ndi mzake kachiwiri. Ndithudi, chinachake basi—basi—kumangong’amba solo ya munthu pamene iye aganiza zimenezo!

<sup>88</sup> Buddy Robinson wakale, pamene iye anali kumeneko. Ena a inu Anazarene muyenera kuti mumvetse izi. Iye anali kukwera mu Model T Ford yakale, akupita chotsika ulendo womwewu womwe ana a Israeli anabwera. Iye anati, “Ulemelero kwa Mulungu! Imitsani chinthucho, ine sindingathe kupiranso!” Kunja uko, iye anafika, ndipo anazungulira, anazungulira, kuzungulira galimotoyo iye anapita, ndipo anakuwa mwamphamvu momwe iye akanathera. Kotero iye analowa, anati, “Yambani chinthucho kachiwiri, tiyeni tizipita.”

<sup>89</sup> Chinachake chokhuza icho! Aleluya! Ndi chiyani icho? Muli

chakuya mkati *umu* chikuitanira ku Chakuya. M'bale, ine ndikukhulupirira pamene chakuya chiri *munu*, chikuyitana, pali Chakuya kunja uko choti chiyankhire kwa icho. Malingana ngati muli njala mu mtima wa munthu tsopano, kuti uchokepo ndi kukamuchitira chinachake Mulungu, izo zimasonyeza kuti pali chinachake chikukankhira pansu, chikubwera pansu kwa ife. Ife tiri pafupi ndi chinthucho, m'bale. Mvetserani usikuuno! Ine ndikukhulupirira izi, mu Dzina la Ambuye, kuti zinthu zomwe ife tachita ndi zinthu zazing'ono pang'ono ku zomwe Mulungu akukonzekera kuti achite pakali pano. Inu mudzamva za zinthu zazikulu.

<sup>90</sup> Ine ndinamuwona Yoswa tsopano, iye waima pamenepo. Iye adzawoloka bwanji mtsinjewo? Tayang'anani pa iwo. Tsopano, iwo analibe zipirala, zazikulu, zomanga mlatho, zitsulo ndi zinthu, kapena matabwa kuti amangire milatho, mmasiku amenewo. Iwo analibe izo ndi iwo. Koma Yoswa anayang'ana kutsidya la Yordano lamatope, iye anayang'ana kumbuyo uko ndipo iye anawona masauzande awa ndi teni sauzande a Ayuda, iye anati, "Mulungu apanga njira!" Mulungu anali atawalonjeza iwo.

<sup>91</sup> Ndipo ngati Mulungu alonjeza, Mulungu adzasunga Mawu Ake. Ngati Mulungu analonjeza kuti adzakuchizani inu, Iye adzachita zimenezo. Ngati Mulungu analonjeza kuti adzakupatsani inu Mzimu Woyera, Iye adzachita zimenezo. Inu mungobwera ndi kudzakhala . . . lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kumukhulupirira Iye, ndipo muwone zimene ziti zichitike. Ndiko kulondola, inu mudzadzazidwa ndi Mzimu Woyera! Mulungu ndi wokakamizika ku Mawu Ake. Iye sangakhoze kutengera Mawu Ake mmbuyo. Iye ayenera kusunga Mawu Ake, kuti akhale Mulungu. Iye ayenera kutero.

<sup>92</sup> Tsopano zindikirani Yoswa atayima pamenepo, anayang'anaponse pozungulira. Oh, mai!

<sup>93</sup> Ife tidzayima pamenepo, nafenso, limodzi la masiku awa. Ife tidzaima kumapeto kwa msewu, pamene mu Yordano wamatope . . . Ndiwe wathanzi usikuuno, mzanga, pakhoza kukhala kuti palibe vuto ndi iwe. Koma limodzi la masiku awa adotolo adzakhala ali mchipinda chako, ndipo adzakuti, "Palibenso chirichonse chimene chingakhoze kuchitidwa." Kugunda kumeneka kudzakhala kukuseserekerana mu mkono. Masiku aunyamata amenewo apita. Chinachake chakantha. Dokotala akuti, "Palibe chimene tingakhoze kuchita. Pepani. Iye ndi mkazi wamng'ono," mnyamata wamng'ono, wamkulu kapena wamng'ono, aliyense yemwe ali, "koma palibe chimene tingachite." Akuyenda kutuluka mchipindamo, inu mudzamverera nthunzi yozizira ya imfa ikuyandama mchipindamo, Yordano wakaleyo adzawoneka wamatope ndi wovuta. Oh, mai!

<sup>94</sup> Ndiye inu mudzakhala monga Yoswa, iye anayang'ana, atakhala kumbuyo uko pa phiri, ndipo pamenepo panali Likasa la pangano, Mkhlapakati. Iye anali ndi Chinachake chimene chimapita pakati pa iye ndi mavuto amenewo.

<sup>95</sup> Ndipo, usikuuno, ife tiri ndi Likasa, Khristu Yesu, Amene wayima pakati pa ife ndi imfa. Ena a masiku awa pamene mpweya womaliza uzidzachoka mthupi mwathu, ine ndikufuna ndidzathamangire ku mtsinje, ndi kukati, "Pereka njira, Yordano, ine ndikupita kukawawona Ambuye wanga." Ine ndikukulupirira Nyenyezi ya Mmawa idzatulukira, kutsika kudzadutsa mzigwa za mthunzi wa imfa, kudzawalitsira njirayo, ndipo Mzimu Woyera udzatabasula mapiko awiri onyezimira kuwoloka Yordano ndi kudzanyamula miyoyo yathu yotopa kupita nayo ku Dziko labwinolo. Ameni. Tsopano zindikirani izi.

<sup>96</sup> Ndiye pamene Yoswa anayang'ana, iye anatenga Likasa la chipangano, anawauza iwo, anati, "Dzisonkhanitseni nokha kunja kuno, dziyeretseni nokha motsutsa mawa, ndipo konzekerani, pakuti inu mudzawona Ulemelero wa Mulungu." Ndiye iye anadziwa kuti Mulungu anali ndi iye.

<sup>97</sup> Atatero iye anatenga ansembe, ndipo iwo anamuika Mulungu patsogolo; Likasalo pamaso pa ansembe, pamaso pa khamulo, anawapanga iwo kukhala mmbuyo mtunda winawake mpaka Likasalo lidutse poyamba.

<sup>98</sup> M'bale, mlongo, ngati inu muti muyike Mulungu patsogolo mu chirichonse chimene inu mukuchita, inu muyenera kuti mudzatuluka bwino. Mumuike Mulungu poyamba.

<sup>99</sup> Ndipo iwo anapita, atanyamula Likasa. Ndipo pamene mapazi a ansembe anadzaponda m'madzi, Mulungu anayalulira mmbuyo mtsinje wa Yordano. Iwo unasunthira mmbuyo. Iye anayima mu Lawi, ndipo Israeli anawoloka pa nthaka yowuma. Anamanga msasa wawo.

<sup>100</sup> Yoswa anali akuyendayenda, masiku angapo kenako, akungoyang'ana pa malowo. Chirichonse chinali chotsekedwa kumtunda uko, chifukwa kumeneko Mulungu anali ataika mantha pa iwo onse, okhala ku Palestina uko kuzungulira Yeriko. Yoswa anali akuyenda kumeneko, ndipo iye anayang'ana, iye anamuwona Winawake. Iye anasolola lupanga lake, iye anati. . . Ndipo Munthu wina uyu anasolola lupanga Lake. Iye anati, "Inu ndinu wa Ndani? Kodi Inu muli wa ife kapena Inu muli wa adani athu?"

<sup>101</sup> Iye anati, "Ayi, koma Ndine Kaputeni wa Khamu la Ambuye. Vula nsapato kumapazi ako, chifukwa malo amene waimapowo ndi malo oyera." Iye anakomana ndi Yesu kumeneko, maso ndi maso, Kaputeni wa Khamu la Ambuye. Ndipo Iye anamuiza iye choti achite, kuti aziguba mozungulira makoma, nkuwomba lipenga, nkudzafuula, ndipo makoma a Yeriko akanadzagwa. Ndipo iwo anatenga dziko la Palestine, anadzakhala mmenemo

monga Mulungu anawalonjezera iwo, chifukwa lonjezo la Mulungu linali la iwo.

<sup>102</sup> Tsopano, m'bale wanga, usikuuno ife tiri pa njira yathu waku Dziko lolonjezedwa. M'mphindi pang'ono ife tikhala tikuyika anthu pano mu dziwe laubatizo ili, ku chikhululukiro cha machimo awo, akukhulupirira pa Ambuye Yesu. Ndipo ine ndikufuna kunena izi, ngati inu simunapange kuyitanidwa ndi kusankhidwa kwanu kukhala kotsimikizika, mwa Khristu, mulole inu mupange izo usikuuno. Inu musatero. . . Inu munene kuti, "Chabwino, M'bale Branham, Mulungu sakundifuna ine, ine sindine woyenera kanthu." Inde, inu muli.

<sup>103</sup> Osati kale kwambiri ine ndinali nditaima ku nyumba yazamakezana mu Tennessee, ndipo ine ndinali kuyang'ana pa zinthu zosiyanasiyana, ndipo ine ndinawona kusanthula kwa thupi la munthu, la munthu yemwe amakhoza kulemera mapaundi fifite. Inu mukudziwa kuti iye anali wochuluka bwanji, kuti mtengo wake unali bwanji? Masenti eyite-foro, phulusa lakelo, masenti eyite-foro. Thupi la munthu kumalemera mapaundi handiredi fifite, mtengo wake kukhala masenti eyite-foro, phulusa lakelo. Pafupifupi kashiamu wokwanira kuti uchitire chinthu chinachake, ndi njereza wokwanira kuwaza chisa cha nkuku ndi zina zotero monga choncho, basi kanthu kakang'ono konse komwe inu munali nako, masenti eyite-foro. Koma inu mumavala chikhotho chaubweya cha madola handiredi kuveka masenti eyite-foro amenewo, kudzutsa mphuno yanu mmwamba mu mlengalenga ndi kumayenda ngati kuti inu munali winawake, chipewa cha madola fifite pamwamba pa masenti eyite-foro amenewo. Panali munthu anaima pamenepo, anati, "Munene kuti, sindife ofunikira mochulukuka kwambiri, kodi ndi choncho, George?"

<sup>104</sup> Ine ndinatembenuka mozungulira, ine ndinati, "Koma, mnyamata, thupi lako liribe mtengo wochulukuka kwambiri, koma uli ndi solo mtengo wake maiko teni milioni. Nanga bwanji zimenezo?" Iye anali akusonyeza akatumba ake, momwe iye analiri wojintcha. Ine ndinati, "Nanga bwanji zimenezo?" Munthu amakonda kubwekerera pa chimene iwo ali.

<sup>105</sup> Osati kale kwambiri, uko Kumadzulo, ine ndinali ndi msonkhano. Ine ndinapita kunyumba ndi mlimi wakale kuti tikadye chakudya chamadzulo. Oh, ndipo ena a anthu ake anali atachiritsidwa. Iye anali atandipatsa ine cheke kumeneko chimene chikanandigulira ine forte-faivi a makachisi awa, ngati ine ndikanafuna. Ine ndinati, "Ine sindikufuna ndalama zanu."

Howard, mchimwene wanga, anali ndi ine, anati, "Bill, bwanji iwe sunatenge cheke chimenecho?"

Ine ndinati, "Ine sindikufuna ndalama zake." Ndiloleni ine ndikhale ndi moyo tsiku ndi tsiku. Osati ndalama nzomwe ine

ndimazitsatira. Ndine mmodzi woti ndiziwatumikira Ambuye Yesu.

<sup>106</sup> Iye anayima pamenepo pamene mkazi ameneyo anachiritsidwa kutali uko, Melikians, mu California. Inu munaziwona izo apa mu pepala laku Louisville. Pamene iwo anabwera kuno, awiri a nthumwi zimenezo, ndipo anabweretsa madola milioni, faivi handiredi sauzande, ndipo ankapereka iwo kwa ine pamene ine ndimakhala mnyumba ya zipinda ziwiri izi. Ine ndinati, “Ine sindikufuna ngakhale kuyang’ana pa iwo. Ayi, bwana. Ayi, bwana.” Chikondi cha ndalama ndi muzu wa choipa chonse. Muzikhala kutali ndi zinthu zimenezo.

Woweta ziweto uyu anatulukira kumeneko, iye anati, “M’busa Branham?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Inu mukuwawona mapiri amenewo kutsidya uko?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

“Inu mukuganiza kuti iwo ali kutali bwanji?”

Ine ndinati, “Ine sindikudziwa.”

Anati, “Iwo ndi mailosi eyite.” Anati, “Ndine mwini mpaka kumeneko, ndi kupitirira kumeneko. Ndi malo anga odyetserako ziweto.”

Ine ndinati, “Mai, izo nzodabwitsa.”

<sup>107</sup> Iye anati, “Ine ndikuwona kumusi uko. Mukuwona mzinda uwo?” Iye anati, “Ine ndine mwini wa banki mu mzinda umenewo; ine ndi mwini wa malo onse awo kumusi *uko*, ndipo ndine mwini mbali *iyi*.” Oh, zonsezo zinali zake!

<sup>108</sup> Anayima, mu ngolo yake yaying’ono. Ine ndinayang’ana pa iye, munthu wabwino kwambiri. Ine ndinaika dzanja langa pa phewa lake, ine ndinati, “M’bale, ine ndikufuna ndikufunsemi inu funso.”

Iye anati, “Chabwino.”

Ine ndinati, “Yang’anani mmwamba momwe mbali *Iyi* uku. Kodi muli ndi zingati kumwamba *Uko*?” Mukuona?

Iye anati, “M’bale Branham, ine ndikuwopa kuti ine ndiribe chirichonse.”

<sup>109</sup> Ine ndinati, “Kumeneko ndi kumene chuma changa chiri tsopano. Ine ndiribe kalikonse pansi pano. ‘Kaya ndiri ndi hema kapena kanyumba, ndi zachiyani kuti ndizisamala? Iwo akundimangira ine nyumba yachifumu kumeneko! Miyala ya mtengowapatali ndi diamondi, ndi siliva ndi golide, nkhokwe Zake ndi zodzadza ndi chuma chosaneneka.’” Inde, bwana. Ndi kumene kuli chuma, kumtunda Uko. Ndipo kumene chuma chako chiri, ndi kumene kuli mtima wako.

<sup>110</sup> Iwo anali akutenga chopereka chachikondi nthawi ina cha Gypsy Smith. Ndipo pamene iwo anabwerera mmbuyo kuseri kwa nyumbayo, kuti apite kunja usiku umenewo, uko kunali mtsikana wamng'ono wosauka wansanza atayima pamenepo. Iye anali yense. . . Zovala zake zonse zinali zitang'ambika pa iye. Iye anali ndi chinachake, iye anati ankafuna kuwawona Bambo Smith. Ndiye Gypsy Smith anati, "Iwe ukufuna chiyani, wokonededwa?"

<sup>111</sup> Anati, "Bambo Smith, ine ndinalibe ndalama iliyonse kuti ndikupatseni inu, koma," anati, "pafupifupi mwezi wapitawo inali Khrisimasi, ndipo winawake anandipatsa ine suwiti wamtengo. Ndipo ine ndimakukondani inu kwambiri, Bambo Smith!" Anati, "Abambo anga anapulumutsidwa, iye si chidakhwa tsopano." Anati, "Ine ndinaganiza kuti ine ndikubweretsereni inu suwiti iyi."

<sup>112</sup> Bambo Smith anayitenga iyo mdzanja lake, misonzi inatsikira m' masaya mwawo. Anamusisita iye pa dzanja, iye anati, "Wokonededwa, mu chopereka changa usikuuno muli zokwanira masauzande a madola mmacheke, koma iyi ndi mphatso yayikulu kwambiri yomwe ine ndiri nayo yonse ya iyo. Iyo yachokera mu mtima wako wawung'ono wodzichepetsa." Oh, mai!

<sup>113</sup> Chimene inu muli nacho usikuuno, abwenzi, inu simuli kanthu, mulimonse. Bwanji inu osapereka zonse zomwe inu muli nazo kwa Khristu? Bwerani, tiyeni tiwoloke Yordano uyu. Tiyeni tipite uko ndipo tikatenge dzikolo. Inu mukuti, "Chabwino, m'bale, inu mukudziwa ine ndiri ndi ntchito yabwino mu mzinda uno. Ndine. . . Ndine wa bungwe linalake mu mzinda uno." Inu ndi ndani, mulimonse? Perekani chimene inu muli nacho, kwa Iye. Tiyeni tidzasonkhane pamwamba apa kuzungulira Yordano ndipo tiwoloke usikuuno, tipite ku Dziko lolonjezedwa. Ambuye akuthandizeni inu. Ine ndikupemphera kuti Iye atero, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>114</sup> Ndikukhumba ine ndikanalalikira motalikirapo pang'ono, koma ine ndasasa mawu. Izo ziri bwino. Tiyeni tiweramitse mitu yathu miniti.

<sup>115</sup> Ambuye Mulungu, ife taima pafupi ndi Yordano usikuuno. Mafunde amatope akale akukhavukira kutsidya uko. Ife tikudziwa limodzi la masiku awa ife tiyenera kudzabwera kumeneko. Ndipo ine ndikuzindikira kuti kunja uko, patsogolo pa aliyense wa ife, pali dzenje lalikulu lakuda, khomo lalikulu lakuya limene munthu amalowamo, lotchedwa imfa. Ndipo ine ndikudziwa nthawi iliyonse imene mtima wanga wagunda ine ndiri kugunda kumodzi kuyandikira kumeneko. Ndipo ine ndiyenera kudzabwera kumusi uko, Ambuye. Ndipo mwamuna ndi mkazi aliyense, mnyamata kapena mtsikana mkati muno, ayenera kudzabwera ku malo amenewo. Tatalikirana nako

bwanji, Inu nokha mukudziwa. Koma, Ambuye, ine sindikufuna kubwera kumeneko ngati wamantha, ine sindikufuna kubwera kumeneko ndikukuwa, “Ambuye, ndipatseni ine masiku angapo kuti ndilape.”

<sup>116</sup> Ine ndikufuna kuti ndidzabwere ngati ngwazi. Ine ndikufuna kudzabwera monga Paulo wakale, ndikunena chinthu chimodzi ichi, “Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Osati pogwirana chanza ndi mlaliki wina, osati polemba dzina langa pa bukhu la mpingo, ndi madontho pang’ono a madzi atakonkhedwa pamwamba pa mutu wanga. Ine ndikufuna kuti ndimudziwe Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake, kuti, pamene Iye adzaitana dzina langa, ine ndidzabwera kuchokera pakati pa akufa. O Mulungu, mulole icho chikhale chokhumba cha mtima uliwonse pano usikuuno.

<sup>117</sup> Ngati pali amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana pano, amene sakukudziwani Inu mu kukhululukidwa kwaulele kwa tchimo, ndipo ali nawo maina awo atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, mulole iwo apange chigamulo chawo pakali pano. Perekani izi, Atate. Ife timawakonda anthu. Ndipo Inu mwatsimikizira mautumiki Anu konsekonse. Ndipo ife tikudziwa kuti Inu muli pano.

Ndipo ife tikuganiza za Israeli akuwoloka Yordano. Chifukwa chiyani? Inu munalonjeza izo kwa iwo, Inu munapereka izo kwa iwo.

Ndipo Inu mupereke izo kwa ife. Ambuye, mulole ife tiwuke ndi kupita kukatenga chuma chathu usikuuno. Perekani izi, Ambuye.

<sup>118</sup> Pamene ife tiri ndi mitu yathu pansi. Ine ndikudabwa ngati pali munthu muno usikuuno anganene kuti, “M’bale Branham,” ndikudzipereka kuchokera mu mtima mwathu, “Ine—ine ndikufuna ndiwoloke Yordano. Ine ndikufuna kuwoloka, koma sindikulondola ndendende panobe. Ine sindine woyenera kuti ndipiteko. Ine ndikanadana nazo kuti ndidzakumane nawo Ambuye mu chikhalidwe changachi. Ine ndikweza mmwamba dzanja langa ndikuti, ‘Ndipemphererene ine, M’bale Branham.’ Ndipo inu muchite zimenezo, mutero inu?” Ine ndichita zimenezo. Kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu ndi ndani? Mulungu akudalitseni inu. Mai, manja angokwera mmwamba paliponse! Winawakenso kwezani manja anu mmwamba, “M’bale Branham, mundipempherere ine.” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata. Mulungu akudalitseni inu, bambo. Ndipo inu kumbuyo uko. Chabwino, winawakenso ikani manja anu mmwamba.

<sup>119</sup> Tsopano penyani, anthu, uwu ukhoza kukhala msonkhano wotsiriza wa Uthenga umene inu mudzakhalemo. Pamene ine

ndichoka ndi kudzabwerera, mkazi wanga amati, “Bill, iwe ukumudziwa *Wakuti-ndi-wakuti?*”

“Inde.”

“Two anafa. *Uyu* anaphedwa. *Uyo* anapita ndi nthenda ya mtima.”

“Oh, iwe sukutanthauza zimenezo?”

“Inde.”


<sup>120</sup> “Oh!” Ine ndikuganiza, “Oh, mai! Ine ndikukumbukira ine ndinaitanira kuguwa nthawi ina, ndipo ndinamuwona bambo ameneyo atakhala pamenepo. Ine ndinkamufuna iye kuti. . .” “Meda,” ine ndinati, “kodi aliyense akudziwa, kodi iye anapulumutsidwa?”

<sup>121</sup> “Ayi, iye anangofa mwadzidzidzi, akubwera kuchokera ku ntchito. *Iye* anayamba kuvala nsapato zake, iye anafa. *Iye* anaphedwa pa ngozi. *Iye* sanadzuke konse ku, tulo take, iye anapita kukagona usiku wina ndipo sanadzuke konse.”

Ine ndikuganiza, “Oh, mai! Ine ndinalalikira kwa mwamuna ameneyo, mkazi ameneyo, achinyamata, nawonso.”

<sup>122</sup> Tsopano musaweruze zinthu molakwitsa, mzanga. Kodi ndinu wochimwa kwenikweni usikuuno? Tsopano mveterani, ngati inu simunabadwe mwatsopano, inu mukadali kutali ndi Khristu. Kodi inu mukufuna kuti mumulandire Iye? Ngati inu mungatero, ndi angati a inu mukufuna kuti mumulandire Iye? Ife tiribe malo pano, ine sindikuganiza, oyitanira anthu kuguwa kuzungulira kuno. Koma ngati inu mungaimirire pa mapazi anu, ndi kuti, “M’bale Branham, poimirira, ine ndikupereka umboni uwu, Ine ndikufuna kuti ndimulandire Khristu pakali pano ngati Mpulumutsi wanga. Ine ndikufuna kuchoka ku chikhalidwe chakale chomwe ine ndikukhalamo.”

<sup>123</sup> Kodi inu mungakhale woonamtima mokwanira mu mtima mwanu, kuti muimirire pa mapazi anu? Ndani ati akhale woyamba kuchita izi, kunena kuti, “Ine ndikufuna kuvomereza”? Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Pali amuna atatu aimirira, mphindi chabe. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ingokhalani chiyimire ngati inu mungathe, dona, ngati inu mungathe. Mulungu akudalitseni inu. Winawakenso. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitse iwe, mwana. Winawakenso. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Winawakenso imirirani pa mapazi anu, ndikuti, “Ine ndikufuna kumulandira Khristu pakali pano. Ine ndikufuna kuchoka mu chikhalidwe changa.” Mulungu akudalitseni inu, bwana. Winawakenso. Mulungu akudalitseni inu ndi dzanja lanu lokwezedwa, kumbuyo uko ndi mwanayo. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ingokhalani chiyimire. Winawakenso imirirani mwamsanga ndithu tsopano. Nanga bwanji kuno, ndi ena a inu ana aang’ono kuno? Inu, dona wamng’ono, Mulungu akudalitseni inu,

mlongo. Mulungu akudalitseni inu pamenepo. Ingokhalani chiyimire, ngati inu mungathe. Mulungu akudalitse iwe, mtsikana wamng'ono. Winawakenso akufuna kuti amulandire Khristu, imirirani. Uko nkulondola. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Imirirani. Winawakenso akuti, "Ine tsopano ndikufuna kumulandira Khristu pakali pano. Ine ndikufuna inu mundikumbukire ine, M'bale Branham, pakali pano." Kodi inu mungaime? Ndikuyembekezera pa inu. "Ine ndikufuna kuti ndimulandire Khristu." Kodi inu mukudziwa kuti ndinu wochimwa, kapena ndi kukaikira basi . . . ? . . . 

53-0329 Israeli Ndi Mpingo #5  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)